Okondedwa wathu Mneneri صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanena kuti, kudzichepetsa kumachokera ku imān (Chikhulupiriro).’ (*Musnad Abī Ya’lā, vol. 6, p. 291, Ḥadīš 7463*) monga momwe imān imamuteteza msilamu kuchita ukafr (kusakhulupirira), Kudzichepetsa kumateteza Munthu kusamvera. Izi zikufotokozeredwanso munkhani yochokera kwa Sayyidunā Ibn ‘Umar رَضِيَ اللهُ عَنْهُمَا: ‘mopanda chikaiko, Kudzichepetsa komanso imān zimagwirizana chimodzi chikasiyidwa china chimachosedwaponso.’ (*Al-Mustadrak lil-Ḥākīm, vol. 1, p. 176, Ḥadīš 66*)

Ntchito zakupembeza

Wuḍū



Kapangidwe ka wuḍū

- ❖ Okonedwa ana, zili zokonedwa kukhala pamalo okwera moyang'ana ku Qiblah popanga wudu.
- ❖ Pangani cholinga (Niya) yotsatirayi musanapange wudu, 'Ndikuchita wudu kuti ndikwaniritse lamulo la Allah عَزَّوَجَلَّ ndikupeza malipiro.'
- ❖ Ndi Sunnah kuwerenga بِسْمِ اللَّهِ musanapange wudu.
- ❖ Ngati kuli kotheka, werengani بِسْمِ اللَّهِ وَالْحَمْدُ لِلَّهِ, monga momwe angelo adzakhala akulembabe zabwino m'Buku la zochita zanu ngati wudu wanu udzakhlapobe.
- ❖ Sambisani manja onse awiri mpaka katatu ndikuchita khilāl (mwachisanzo kudusitsa zala za mmanja muzinzke).
- ❖ Tsopano gwiritsani ntchito miswāk molingana ndi Sunnah.

- ❖ Tsopano tsukani pakamwa panu katatu ndikuchukucha ngati simusala kudya.
- ❖ Tsopano kokera madzi katatu. Ngati simusala, kokera madzi mpaka pamwamba pa fupa lofewa la mkati la mphuno. Tsopano yendesani mkati mwa mphuno ndi chala chaching'ono cha dzanja lamanzere.
- ❖ Sambisani nkhope yonse katatu kuti madzi ayende mbali iliyonse kuchokera pamwamba pa mphumi mpaka pansu pa chibwano komanso kuchokera ku khutu kupita ku linzake.
- ❖ Tsopano sambisani nkono wa manja kuchokera ku nsonga kwa zala mpaka (ndi kuphatikizapo) mu chigongono katatu kuti pasakhale malo kuchokera pachigongono kupita ku misomali kukhala osanyowa. Kenako sambisani nkono wamanzere chimodzimodzi.
- ❖ Tsopano nyowetsani manja onse ndikudutsitsa pamutu wonse.
- ❖ Tsopano yendesani chala cha mkamba phala mkati mwa makutu ndikuseli kwake ndi chala chachikulu. Mudzayendesanso kumbuyo kwa khosi ndi kuseli kwa manja.
- ❖ Tsopano sambisani mapazi onse katatu mpaka (kuphatikiza) m'miyendo. Tsukani phazi lakumanja kaye kenako lamanzere. Komanso chitani khilāl (mwachisanzo kudutsitsa chala chaching'ono chakumanzere m'mipata ya zala za mapazi onse awiri).

Ziphunzitso zofunika za chisilamu (Gawo II)

- ❖ Yambani khilāl kuchokera ku chala chaching'ono cha phazi lakumanja ndikumalizitsa pachala chaching'ono chakumanzere.

Chidziwitso: Atsogolereni ana pachiwonetsero pakuwa thandizira mmalo ochitira wuḍū ndikuwalangiza kuti asawononge madzi.

Hujjat-ul-Islam Imām Muhammad Ghazālī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ wati, ‘Pamene akusambitsa chiwalo chilichonse, ayembekezere kuti machimo ake achotsedwa m’chiwalocho’.¹

- ❖ Komanso aziwerenga du’a iyi pambuyo pa wudu (ndi ṣalāt-‘alan-Nabī صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ kamodzi asanawerenge ndipo kamodzi kumapeto):

اللَّهُمَّ اجْعَلْنِي مِنَ التَّوَّابِينَ وَاجْعَلْنِي مِنَ الْمُتَطَهِّرِينَ

Kumasulira: E, Allah (عَزَّوَجَلَّ)! Ndichiteni kukhala m’gulu la amene alapa kwambiri, ndipo ndikhazikitseni kukhala m’gulu la oyeretsedwa.²

Zitseko zonse zisanu ndi zitatu za Paradiso zimatseguka

Hadiš ina ikunena kuti, ‘Munthu amene amapanga wudu moyenera nkuyang’ana kumwamba ndikuwerenga Kalimaḥ Shaḥādaḥ, makomo onse asanu ndi atatu a Paradiso amam’tsegukira. Akhoza kulowa pa khomo lililonse limene akufuna.’³

¹ Iḥyā-ul-‘Ulūmiddīn, Kitāb Asrār-uṭ-Ṭahārah, vol. 1, pp. 183

² Iḥyā-ul-‘Ulūmiddīn, Kitāb Asrār-uṭ-Ṭahārah, vol. 1, pp. 184

³ Sunan-ul-Kubrā lin-Nasāi, Kitāb ‘Amal-ul-Yawm wal-Laylāh, vol. 6, pp. 25, Ḥadiš 9912

Kupambana kowerenga Surah Qadr pambuyo pa wudu

Haadis ina ikulongosola: “Ngati munthu awerenga Surah Qadr kamodzi pambuyo pa Wudu, adzakhala m’gulu la ma siddiqin, ndipo ngati aiwerenga kawiri, adzakhala m’gulu la ma shuhada, ndipo ngati aiwerenga katatu adzakhala m’gulu la aneneri عَلَيْهِمُ السَّلَامُ pa tsiku lachiweruzo.¹

Maso sadzakhala opanda mphamvu

Ngati munthu atayang'ana kumwamba pambuyo pochita wudu ndikuwerenga Sūrah Qadr, maso ake sadzafowoka, إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ.

Tanthauzo la ‘kusambisa’

Kusambitsa chiwalo cha thupi kumatanthauza kuti kuyenda kwa madontho awiri amadzi pa gawo lonse la thupi. Ngati angonyowetsedwa ndi kupaka dzanja lonyowa pamwamba pake, kapena ngati yatsikira dontho limodzi lamadzi pamwamba pake, ndiye kuti siidzaonedwa ngati yosambitsidwa, ndipo wudu kapena ghushl siwudzatheka.

Azān

Funso 1: Kodi azān ndi chani?

Yankho: Kulengeza kwa mtundu wina wapaderadera komwe kumayitanira Asilamu ku ṣwalāh kumatchedwa kuti azān.

Funso 2: Kodi kuchita azān ndi Fard?

¹ Kanz-ul-‘Ummāl, vol. 9, pp. 132, Ḥadiṣ 26085

Yankho: Ayi, kuchita azān ndi sunnah muakkadaḥ kwa ṣalāḥ zisanu za Fard zopempheredwa pa jamā’at mu nzikiti.

Funso 3: Kodi tingawerenge ṣalāt-‘alan-Nabī ﷺ tisanapange azān?

Yankho: Inde, kuwerenga ṣalāt-‘alan-Nabī ndi ntchito ya malipiro صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ tisanachite azān.

Funso 4: Kodi tiyenera kuchita chani pamene azān akunenedwa?

Yankho: Tiyenera kusiya kukambirana kwathu ndi zochita zina zonse polemekeza azān ndi kuyankha.

Funso 5: Kodi mawu a azān ndi ati?

Yankho: Mawu a azān ndi awa:

اللَّهُ أَكْبَرُ	اللَّهُ أَكْبَرُ
اللَّهُ أَكْبَرُ	اللَّهُ أَكْبَرُ
أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ	أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ
أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولُ اللَّهِ	أَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا رَسُولُ اللَّهِ
حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ	حَيَّ عَلَى الصَّلَاةِ
حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ	حَيَّ عَلَى الْفَلَاحِ
اللَّهُ أَكْبَرُ	اللَّهُ أَكْبَرُ
لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ	

Malamulo oyamba a salaḥ

Funso 1: Kodi pali malamulo oyamba angati a swalaḥ?

Yankho: Pali malamulo oyamba asanu ndi limodzi a salaḥ:

(1) Ṭaḥārat (ukhondo) (2) Satr awrat (kuphimba maliseche) (3) kuyang'ana ku Qiblah (Istiqbāl Qiblaḥ)(4) nthawi (Waqt) (5) cholinga (Niyyat) (6) kuchita Takbīr yoyamba (Takbīr Taḥrīmaḥ)

Funso 2: Kodi ukhondo (Taḥārat) umatanthauza chani?

Yankho: pa thupi, zovala ndi malo oswalira akhale oyera ku zonyansa zamtundu uliwonse.

Funso 3: Kodi tanthauzo la satr 'awrat' ndi chani?

Yankho: Thupi la mwamuna liyenera kukhala lophimbidwa kuyambira pa mchombo mpaka m'mawondo, pamene thupi lonse la mkazi liyenera kukhala lophimbidwa kupatula zigawo zisanu izi: nkhope, zikhato zonse ziwiri, pansu pa mapazi onse awiri.

Funso 4: Kodi istiqbāl Qiblaḥ imatanthauza chani?

Yankho: Istiqbāl Qiblaḥ kutanthauza kuti kuyang'ana ku Qiblaḥ pa nthawi ya swala.

Funso 5: Kodi mawu akuti waqt (nthawi) amatanthauza chani?

Yankho: Mawu akuti Waqt akutanthauza kuti ndikofunikira kupephera ṣwalaḥ munthawi yake.

Funso 6: Kodi mawu akuti niyyat (cholinga) akutanthauza chani?

Yankho: Mawu akuti Niyyat akutanthauza kuti cholinga chokhazikika mu mtima. Kupanga cholinga chapakamwa sikofunikira. Komabe, cholinga chapakamwa pamodzi ndi cholinga cha mtima ndicho chabwino.

Funso 7: Kodi mawu oti Takbīr Taḥrīmah akutanthauza chani?

Yankho: Kunena Takbīr poyambirira (الله أكبر) ndicholinga choti uyambe ṣwalāh kumatchedwa ‘Takbīr yoyamba (Takbīr Taḥrīmah)’.

Zikakamizo za salāh (Faraid)

Funso 1: Kodi pali ma farāiḍ a ṣalāh angati?

Yankho: Pali ma farāiḍ asanu ndi awiri a Swalah:

(1) Takbīr Taḥrīmah (2) Qiyām (3) Qirā-at (4) Rukū’ (5) Sajdah (6) Qa’daḥ akhīrah (7) Khurūj bi ṣun’ihī.

Funso 2: Kodi mawu oti Takbīr Aūlā amatanthauza chani?

Yankho: Mawu oti Takbīr Taḥrīmah amatchedwanso Takbīr Aūlā. Ndilo lamulo lomaliza pamalamulo oyamba a ṣwalāh koma ndi lamulo loyamba mu mafarāiḍ a Swalah. Kunena Takbīr (الله أكبر) kuti ayambe ṣalāh kumatchedwa Takbīr- Taḥrīmah kapena Takbīr Aūlā.

Funso 3: Kodi mawu oti qiyām amatanthauza chani?

Yankho: Kuima molunjika mutanena Takbīr Taḥrīmah kumatchedwa qiyām. Nthawi ya qiyām ndi yofanana ndi ya Qirā-at.

Funso 4: Kodi tanthauzo la qirā-at ndi chani?

Yankho: Kutchula chilembo chilichonse kuchokera pamalo ake olondola kumatchedwa qirā-at. Powerenga motsitsa mawu, ndikofunikira kuti owerengayo azizimva kuwerenga kwake.

Funso 5: Kodi mawu oti rukū' amanthauza chani?

Yankho: Pambuyo pochita qirā-at, kuchepa kwa rukū' ndikuwerama chatsogolo mpaka kufika mmawondo. Kwa munthu wammuna, rukū' yathunthu ndiyo kusunga msana mowongoka.

Funso 6: Kodi mawu akuti sajdāh akutanthauza chani?

Yankho: Pambuyo pochita rukū', kupanga mafupa asanu ndi awiri kukhudza pansi, mwa chitsanzo manja, mapazi, mawondo ndi fupa la m'mphuno, kumatchedwa sajdāh. Ikani pamphumi molimba kwambiri kuti kuuma kwa nthaka kumveke. Sujud ziwiri zili Fard mu raka'at iliyonse.

Funso 7: Kodi mawu akuti qa'daḥ akhīrah amanthauza chani?

Yankho: Qa'daḥ akhīrah imachitidwa pambuyo pakupempheredwa ma rak'āt a Swalah. Kukhala pa Tashāḥhud (التَّحِيَّات) mpaka pa عَبْدُاُورَسُوْلُهُ kukawerengedwa kumatchedwa qa'daḥ akhirah, ndipo imeneyi ndi Farad.

Funso 8: Kodi khurūj bi ṣun'ihī ndi chani?

Yankho: Kuchita salamu pomaliza ṣalāh pambuyo pa qa'daḥ akhīrah kumatchedwa khurūj bi ṣun'ihī.

Kapempheredwe ka swalah

Kapempheredwe ka swalâh

- ❖ Imani moyang'ana ku Qiblah muli ndi wudu. Tsopano kwezani manja onse ndi zala zazikulu kukhuza makutu.
- ❖ Manja akakwezedwa, zala zisalumikizidwe pamodzi kapena kotalikana, ndipo zikhato ziyang'ane ku Qiblah.
- ❖ Tsopano pangani chisimikizo cholimba cha Ḥ walâh yomwe mukufuna kupephera. Cholinga chapakamwa ndichabwino.
- ❖ Tsopano pamene mukunena Takbîr Ta Ḥ rîmah (الله أكبر), sitsani manja anu ndi kuwapinda pansu pa mchombo.
- ❖ Tsopano nenani Šanâ motere:

سُبْحَانَكَ اللَّهُمَّ وَبِحَمْدِكَ
وَتَبَارَكَ اسْمُكَ وَتَعَالَى جَدُّكَ وَلَا إِلَهَ غَيْرُكَ

- ❖ Kenako nenani Ta'awwuz:

أَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ

- ❖ Kenako werengani Tasmiyyah:

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

❖ Tsopano werenga Surah Fatihah yonse:

أَحْمَدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ ﴿١﴾ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ﴿٢﴾ مَلِكِ يَوْمِ الدِّينِ ﴿٣﴾ إِيَّاكَ
نَعْبُدُ وَإِيَّاكَ نَسْتَعِينُ ﴿٤﴾ اهْدِنَا الصِّرَاطَ الْمُسْتَقِيمَ ﴿٥﴾ صِرَاطَ الَّذِينَ
أَنْعَمْتَ عَلَيْهِمْ ۗ غَيْرِ الْمَغْضُوبِ عَلَيْهِمْ وَلَا الضَّالِّينَ ﴿٦﴾

❖ Mukamaliza Sūrah Fātiḥah, nenani **أَمِين** (āmīn) motsitsa mawu. Kenako werenga ndime zitatu zazifupi, kapena vesi imodzi yayitali yofanana ndi ma vesi atatu afupi, kapena sura ina iliyonse monga Sūrah Ikhlāṣ.

قُلْ هُوَ اللَّهُ أَحَدٌ ﴿١﴾ اللَّهُ الصَّمَدُ ﴿٢﴾ لَمْ يَلِدْ ۗ وَلَمْ يُولَدْ ﴿٣﴾
وَلَمْ يَكُنْ لَهُ كُفُوًا أَحَدٌ ﴿٤﴾

❖ Tsopano weramani pochita rukū' uku mukunena **اللَّهُ أَكْبَرُ**. Werengani tasbīḥ ya pa rukū', **سُبْحَانَ رَبِّيَ الْعَظِيمِ** katatu kapena kasanu.

❖ Kenako imirirani molunjika kunena tasmī', **سَبَّحَ اللَّهُ لِمَنْ حَمْدَهُ**. Kuyimirira kumeneku kumatchedwa qawmah.

❖ Ngati mukupephera ṣwalāḥ nokha, nenaninso **اللَّهُمَّ رَبَّنَا وَلَكَ الْحَمْدُ**.

- ❖ Kenako gwadani pansu kuti muchite sajdaḥ uku mukunena **اللَّهُ أَكْبَرُ** ndipo zala zonse khumi za mmiyendo ziyang'ane ku Qiblaḥ. Kenako werengani tasbīḥ ya sajdaḥ, **سُبْحَانَ رَبِّيَ الْأَعْلَى**, katatu kapena kasanu.
- ❖ Kukhala pakati pa sujūd ziwirizi kumatchedwa jalsaḥ. Khalani mu jalsaḥ kwa nthawi yonse yomwe **سُبْحَانَ اللَّهِ** atha kunenedwa kamodzi. Kenako pangani sajdaḥ yachiwiri uku mukunena kuti **اللَّهُ أَكْبَرُ**.
- ❖ Rak'at imodzi yamalizidwa. Pepherani rak'at yachiwiri mofanananso.
- ❖ Kukhala pambuyo pa ma raka'at awiri powerenga **التَّحِيَّاتِ** kumatchedwa qa'daḥ.
- ❖ Tsopano werengani Tashahud pa qa'daḥ,

**التَّحِيَّاتُ لِلَّهِ وَالصَّلَاةُ وَالطَّيِّبَاتُ السَّلَامُ عَلَيْكَ أَيُّهَا النَّبِيُّ
وَرَحْمَةُ اللَّهِ وَبَرَكَاتُهُ السَّلَامُ عَلَيْنَا وَعَلَى عِبَادِ اللَّهِ الصَّالِحِينَ
أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَأَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا عَبْدُهُ وَرَسُولُهُ**

- ❖ Mukatsala pang'ono kunena mawu oti 'لا' mu Tashaḥḥud, onesani kuzungulira kwa chala chapakati ndi chala chachikulu chakumanja, ndikupangitsa chala chaching'ono ndi cha mphete kukhudza chikhatho.

- ❖ Kenako kwezani chala chankomba phala kwinaku mukunena kuti ‘لَا’ ndipo chitsitseni kenako tambasulani dzanja pamalo pomwe mukunena mawu oti ‘لَا’.
- ❖ Ngati mukupephera ṣwalaḥ yomwe ili ndi ma rak’āt oposa awiri, imiriraninso uku mukunena Takbīr ‘اَكْبَرُ اللهُ’.
- ❖ Ngati mukupephera swalaḥ farḍ swalaḥ werengani اللهُ بِسْمِ ndi Sūrah Fātiḥah mu qiyām ya rakaat yachitatu ndi yachinayi, koma osonjezeranso sura ina.
- ❖ Kukhala mu qa’daḥ mutapephera ma rak’āt onse kumatchedwa qa’daḥ akhiraḥ.
- ❖ Werengani swalat ya Ibrāḥimī pambuyo pa tashahḥud mu qa’daḥ akhiraḥ.

اللَّهُمَّ صَلِّ عَلَى مُحَمَّدٍ وَعَلَى آلِ مُحَمَّدٍ كَمَا صَلَّيْتَ عَلَى إِبْرَاهِيمَ
وَعَلَى آلِ إِبْرَاهِيمَ إِنَّكَ حَمِيدٌ مَجِيدٌ ۝ اللَّهُمَّ بَارِكْ عَلَى مُحَمَّدٍ
وَعَلَى آلِ مُحَمَّدٍ كَمَا بَارَكْتَ عَلَى إِبْرَاهِيمَ وَعَلَى آلِ إِبْرَاهِيمَ إِنَّكَ
حَمِيدٌ مَجِيدٌ ۝

- ❖ Kenako werengani du’ā māšūrah.

اللَّهُمَّ رَبِّ اجْعَلْنِي مُقِيمَ الصَّلَاةِ وَمِنْ ذُرِّيَّتِي ۖ رَبَّنَا وَتَقَبَّلْ دُعَاءِ ۝
رَبَّنَا اغْفِرْ لِي وَلِوَالِدَيَّ وَلِلْمُؤْمِنِينَ يَوْمَ يَقُومُ الْحِسَابُ ۝ رَبَّنَا
أَتْنَا فِي الدُّنْيَا حَسَنَةً وَفِي الْآخِرَةِ حَسَنَةً وَقِنَا عَذَابَ النَّارِ ۝

- ❖ Kuti mumalize swalah, tembenuza nkhope yanu ku phewa lanu lakumanja ndipo nena **اللَّهُمَّ اجْعَلْنِي مُقِيمَ الصَّلَاةِ وَمِنْ ذُرِّيَّتِي ۖ رَبَّنَا وَتَقَبَّلْ دُعَاءِ ۝**. Kenako tembenezira nkhope yanu ku phewa lanu lakumanzere, ndipo nenani **رَبَّنَا اغْفِرْ لِي وَلِوَالِدَيَّ وَلِلْمُؤْمِنِينَ يَوْمَ يَقُومُ الْحِسَابُ ۝ رَبَّنَا أَتْنَا فِي الدُّنْيَا حَسَنَةً وَفِي الْآخِرَةِ حَسَنَةً وَقِنَا عَذَابَ النَّارِ ۝**.



Na'at

Madanī Madīnay Wālay*



Mujhāy dar pay p̄hir bulānā Madanī Madīnay wālay

Ma-ay 'ishq bhī pilānā Madanī Madīnay wālay

Mayrī ānk̄h mayn samānā Madanī Madīnay wālay

Banay dil tayrā ihikānaḥ Madanī Madīnay wālay

Tayrī jab kay dīd ḥo gī jabhī mayrī Eid ḥo gī

Mayray khuwāb mayn tū ānā Madanī Madīnay wālay

Mujhāy gham satā raḥay ḥayn mayrī jān khā raḥay ḥayn

Tum hī ḥauslah̄ baḥhānā Madanī Madīnay wālay

Mayn agarcheḥ ḥūn kamīnaḥ, tayrā ḥūn Shāḥ-e-Madīnaḥ

Mujhāy qadmon say lagānā Madanī Madīnay wālay

Tayrā tujh̄ say ḥūn suwālī Shāḥā p̄hayrnā na khālī

Mujhāy apnā tū banānā Madanī Madīnay wālay

* Wasāil-e-Bakhshish, pp. 283-288, Multaqaṭan

*Yeĥ marīz mar raĥā ĥay tayray ĥāth mayn shifā ĥay
Ay Ṭabīb jald ānā Madanī Madīnay wālay*

*Tū ĥī Anbiyā kā Sarwar tū ĥī daw jaĥān kā Yāwar
Tū ĥī Raĥbar-e-Zamānaĥ Madanī Madīnay wālay*

*Tū Khudā kay ba'd baĥtar ĥay sabĥī say mayray Sarwar
Tayrā ĥāshmi ĥāranā Madanī Madīnay wālay*

*Tayrī farsh per ĥukūmat tayrī 'Arsh per ĥukūmat
Tū Shaĥanshāĥ-e-Zamānaĥ Madanī Madīnay wālay*

*Yeĥ karam baṛā karam ĥay tayray ĥāth mayn bĥaram ĥay
Sar-e-ĥashr bakhshwānā Madanī Madīnay wālay*

*Shaĥā aysā jazbaĥ pāūn kay mayn khūb sīkh jāūn
Tayrī sunnatayn sikhānā Madanī Madīnay wālay*

*Mayray Ghauš kā wasīlah raĥay shād sab qabīlah
Unĥayn Khuld mayn basānā Madanī Madīnay wālay*

*Tayray gham mayn kāsh! 'Aṭṭār raĥay ĥer ĥārī giriftār
Gham-e-māl say bachānā Madanī Madīnay wālay*

Ngale za Madanī

Ngale za Madanī za kugwirana chanza

- ❖ Akakumana Asilamu awiri, ndi Sunnah kwa iwo kuchita Salam ndi kugwirana chanza manja onse awiri.¹
- ❖ Komanso pangani salamu mukamasiyana. Mukhozanso kugwirana chanza.
- ❖ amene akukondana wina ndi mnzake chifukwa cha chifuniro cha Allah ﷻ kukumana ndi kugwirana chanza wina ndi mnzake, kenako mfunireni zabwino Mtumiki (Swalat) machimo awo akale ndi amtsogolo Amakhululukidwa asanasiyane.²
- ❖ Mukamaliza kuwerenga ṣalāt-‘alan-Nabī ﷺ uku mukugwirana chanza, bwerezaninso du’ā iyi ngati nkotheka:

يَغْفِرُ اللَّهُ لَنَا وَلَكُمْ mwa chisanzo
Allah ﷻ akukhululukireni inu ndi ife.

¹ Ad-Dur-rul-Mukhtār, Kitāb-ul-Ḥaẓr wal-Ibāḥāh, vol. 9, pp. 629

² Musnad Abi Ya’lā, vol. 3, pp. 95, Ḥadiš 2951

- ❖ Du'a yomwe imapangidwa pomwe Asilamu awiri akugwirana chanza imayankhidwa, ndipo onse awiri amakhululukidwa manja awo asanasiyane *إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ*.
- ❖ Kugwirana chanza kumachotsa udani.¹
- ❖ Wokonedwa Mtumiki *صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ* anati: Ngati munthu agwirana chanza ndi m'bale wake wa Chisilamu, ndipo palibe yemwe ali ndi chidani mumtima mwake ndi mnzake, Allah *عَزَّوَجَلَّ*. Adzawakhululukira machimo awo akale manja awo asanalekani. Ndipo amene ayang'ana m'bale wake ndi chikondi, ndipo alibe m'kwiyo mu mtima wake kapena pachifuwa chake, adzakhululukidwa onse awiriwo asanayang'ane kumbali.²
- ❖ Ndi ndizokonedwa kugwirana chanza nthawi iliyonse mwakumana ndi aliyense.³
- ❖ Si Sunnah kugwirana chanza ndi dzanja limodzi lokha. Ndi Sunnah kugwirana manja onse awiri ndi wina ndi mzake.⁴
- ❖ Anthu ena amangokhudza zala zawo kwa anzawo. Iyinso si Sunnah.⁵

¹ Al-Muwattā lil-Imām Mālik, Kitāb Ḥusn Al-Khalq, vol. 2, pp. 407, Ḥadīš 1731

² Kanz-ul-'Ummāl, Kitāb-uş-Şuḥbah, vol. 9, pp. 57, Ḥadīš 25358

³ Rad-dul-Muḥtār, Kitāb-ul-Ḥaḥr wal-Ibāḥāḥ, vol. 9, pp. 628

⁴ Al-Marja'-us-Sābiq, pp. 629

⁵ Al-Marja'-us-Sābiq

- ❖ Ndi makrūh kupsompona dzanja lako pambuyo pogwirana chanza ndi wina.¹
- ❖ Nthawi yogwirana chanza, Sunnaḥ ndi yoti manja a anthu awiri azigwirana wina ndi mnzake popanda choyika pakati, monga mpango kapena china chilichonse.²

Ngale za Madani zodulira zikhadabo



- ❖ Ndi ndizokonedwa kudula zikhadabo Lachisanu. Komabe, munthu sayenera kuyembekezera Lachisanu ngati zikhadabo zake zakula.³
- ❖ Şadr-ush-Sharī'aḥ, Badr-uṭ-Ṭarīqah Maulānā Amjad 'Alī A'zamī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anati: zinanenedwa kuti: aliyense wodula zikhadabo zake pa siku la chisanu adzatetedwa ku masautso mpaka Lachisanu lotsatira ndipo kuonjezera masiku atatu, kutanthawuza masiku khumi onse.' M'nkhani ina, zanenedwa kuti amene adule zikhadabo zake Lachisanu, chifundo

¹ Tabyīn-ul-Ḥaqāiq, Kitāb-ul-Karāhiyah, vol. 7, pp. 56

² Rad-dul-Muḥtār, Kitāb-ul-Ḥaẓr wal-Ibāḥah, vol. 9, pp. 629

³ Bahār-e-Sharī'at, part 16, pp. 225

chidzatsikira [pa iye] ndipo machimo ake adzachotsedwa [mwachisanzo kukhululukidwa].¹

- ❖ Njira yodulira Zikhadabo za manja ili motere: yambani kudula chikhadabo cha chala chakumanja cha nkono wa kumanja ndikupitiriza kudula motsatizana mpaka chikhadabo cha chala chaching'ono, kusiya chala chachikulu cha dzanja lamanja. Kenako yambani ndi chala chaching'ono cha kumanzere ndikupitiriza kudula motsatizana mpaka chachikulu. Pamapeto pake, dulani chala chachikulu cha dzanja lamanja.
- ❖ Palibe kunenedwa kuchokera mu Hadithi zokhuza ndondomeko yodulira zikhadabo za miyendo. Ndi bwino kuzidula kuyambira chala chaching'ono kwambiri cha phazi lakumanja ndikudula zikhadabo motsatana mpaka chikhadabo chachikulu. Kenako yambani ndi chala chachikulu cha phazi lakumanzere ndikudula zikhadabo motsatizana kuphatikizapo chala chaching'ono kwambiri.²
- ❖ Kuluma zikhadabo ndi makrûh ndipo kungayambitse matenda akhate.³
- ❖ Mukamaliza kudula zikhadabozo, zikwirireni kapena zitayeni.
- ❖ Ndi makrûh kuponya zikhadabo zodulidwa mchimbudzi chifukwa zimayambitsa matenda.⁴

¹ Al-Marja'-us-Sābiq, pp. 226

² Al-Marja'-us-Sābiq, pp. 226 to 227

³ Al-Marja'-us-Sābiq, pp. 227

⁴ Bahār-e-Sharī'at, part 16, pp. 231

- ❖ Osadula zikhadabo Lachitatu chifukwa izi zingayambitse leukoderma. Komabe, ngati padutsa masiku 39 kuchokera pamene zikhadabo zinadulidwa komaliza ndipo Lachitatu limakhala tsiku la 40, kutanthauza kuti pakadutsa masiku oposa 40 kuchokera pamene zikhadabozo zinali zosadulidwa, ndiye kuti n’koyenera kudula zikhadabo pa tsiku lomwelo, ngakhale ngati zikhadabozo zinali zosadulidwa. ndi Lachitatu. Dziwani kuti nkosaloledwa komanso makrûh Taḥrīmī kusiya zikhadabo zosadulidwa kwa masiku oposa 40.¹

Chitsanzo Chachikulu Cha kupirira

Sayyidunā Imām Ghazālī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anafotokoza kuti: ‘Munthu anayakhula mwaukali kwa Amīr-ul-Mūminīn Sayyidunā ‘Umar Bin ‘Abdul ‘Azīz رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ. mogwetsa mutu wake, Sayyidunā ‘Umar Bin ‘Abdul ‘Azīz رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anati: “Mukufuna ndikwiye kuti satan andichite ozikweza ndikundipanga ine kukuponderezani chifukwa cha mphamvu zanga, ndikuti muzandibwezere pa tsiku lachiweruzo ? sindizachita izi, atanena izi, anakhala chete’

(Kīmiyā-e-Sa’ādat, vol. 2, p. 597)

¹ Fatāwā Razawiyyāh, vol. 22, pp. 685 Mulakhkhaṣan

Ngale za Madani polowa ndi kutuluka m'nyumba

- ❖ Werengani du'ā iyi musanalowe m'nyumba:

بِسْمِ اللَّهِ وَلَجْنَا بِسْمِ اللَّهِ خَرَجْنَا وَعَلَى رَبِّنَا تَوَكَّلْنَا

Kumasulira: Tikulowa (m'nyumba) ndi dzina la Allah (عَزَّوَجَلَّ) ndikutuluka m'nyumba ndi dzina la Allah (عَزَّوَجَلَّ), ndipo tatsamira kwa Allah (عَزَّوَجَلَّ) Mbuye wathu.¹

- ❖ Gwetsani nkhope mukamalowa m'nyumba.
- ❖ Lowani pogwiritsa ntchito phazi lanu lakumanja kaye.
- ❖ Pangani salam poyamba mukamalowa mnyumba.
- ❖ Komanso pangani salamu potuluka m'nyumba.
- ❖ Tulukani pogwiritsa ntchito phazi lanu lakumanzere.
- ❖ Werengani du'ā iyi pochoka m'nyumba:

بِسْمِ اللَّهِ تَوَكَّلْتُ عَلَى اللَّهِ لَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ ط

Kumasulira: Ine (ndikutuluka m'nyumba yanga) Allah (عَزَّوَجَلَّ), mu Dzina lake (ndipo) Ndikudalira mwa Allah (عَزَّوَجَلَّ). Kutha kudziletsa kumachimo ndi kutha

¹ Sunan Abī Dāwūd, Kitāb-ul-Adab, vol. 4, pp. 420, Ḥadīṣ 5096


*kuchita zabwino ndi kwa Allah عَزَّوَجَلَّ basi.*¹

Ngale za Madani zovalira Nsapato

- ❖ Gwedezeni nsapato musanavale.
- ❖ Werengani بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ musanavale nsapato.
- ❖ Choyamba valani nsapato yakumanja kenako yamanzere.
- ❖ Choyamba chotsani nsapato yakumanzere kenako yakumanja
- ❖ Osayenda mutavala nsapato imodzi yokha. Muvale kapena chotsani zonse ziwiri.
- ❖ Chotsani nsapato mukakhala pansu.

Ngale za Madani povala zovala

- ❖ Chovala choyera ndi chabwino kuposa zovala zina zonse.
- ❖ Mukamavala Buluku, izilekeza pamwamba pa akakolo kuti awoneke.
- ❖ Mukamavala zovala, yambani ndi mbali yakumanja.



¹ Sunan Abi Dāwūd, Kitāb-ul-Adab, vol. 4, pp. 420, Ḥadīṣ 5095

- ❖ Choyamba ikani dzanja lamanja kunkono wamanja wa kurta, ¹ kenako ikani dzanja lamanzere la nkono wa kumanzere.
- ❖ Chimodzimodzi, choyamba ikani phazi lakumanja mumwendo wa kumanja wa Buluku, ndiyeno ikani phazi lakumanzere mu mwendo wa kumanzere.
- ❖ Povula zovala, yambani ndi kumanzere.

Ngale za Madani pogwilitsa ntchito kohl

- ❖ Kohl yabwino kwambiri ndi 'išmid'. Imakulitsa kuona kwa maso komanso imakulitsa nsidze. ²
- ❖ Ndikololedwa kugwiritsa ntchito kohl yopangidwa ndi miyala. Kwa amuna kugwiritsa ntchito kohl wakuda ndi cholinga chokongola ndi makrūh. Koma akaigwiritsa ntchito popanda cholinga chokongola, si makrūh. ³
- ❖ Ndi Sunnah kugwiritsa ntchito kohl musanagone. ⁴
- ❖ Nayi chidule cha njira zitatatu zomwe zanenedwa zogwiritsa ntchito kohl:

¹ A long loose full-sleeved shirt.

² Sunan-ut-Tirmiẓī, Kitāb-ul-Libās, vol. 3, pp. 293, Ḥadiṣ 1763

³ Fatāwā Ḥindiyyah, Kitāb-ul-Karāhiyah, vol. 5, pp. 359

⁴ Al-Marja' -us-Sābiq, pp. 294

1. Nthawi zina, ikani kohl m'maso onse katatu.
2. Nthawi zina, ikani kohl katatu m'diso lakumanja komanso kawiri kumanzere.
3. Ndipo nthawi zina, ikani kohl kawiri m'maso onse, ndipo pamapeto pake, gwiritsani ntchito singano wa kohl kuti mugwiritsenso ntchito m'maso onse awiri.¹

Ngale za Madanī popaka mafuta patsitsi

- ❖ Nenani بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ musana pake mafuta kutsitsi.
- ❖ Gwirani botolo ndi dzanja lanu lamanja ndikutsanulira mafutawo pachikhatho cha dzanja lanu lamanzere.
- ❖ Choyamba, pakani mafuta ku nsidze yakumanja kenako kumanzere, pogwiritsa ntchito chala cha dzanja lanu lamanja.
- ❖ Kenako, pakani mafuta mu msize zakumanja ndi kumanzere.
- ❖ Kenako werengani بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ndipo pakani mafuta tsitsi lanu.

¹ Sunnatayn aur Ādāb, pp. 58

Ngale za Madani pakupesa tsitsi

- ❖ Werengani poyamba بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِیْمِ.
- ❖ Ndi Sunnah kupesa tsitsi kuchokera mbali yakumanja.¹
- ❖ Choyamba pesani nsidze yakumanja kenako yakumanzere.
- ❖ Tsopano pesani kumanja kwa tsitsi kenako kumanzere.

Miyambo popita kuchimbudzi

- ❖ Lowani ku bafa pogwiritsa ntchito phazi lanu lakumanzere kaye.²
- ❖ Osachotsa buluku ndi zina m'thupi mpaka mutatsala pang'ono kukhala, ndipo musawonetse gawo lochulukirapo la thupi kuposa momwe limafunikira.³
- ❖ Osakodza uli chiimire ndi makruh.⁴
- ❖ Ndi makruh kukodza pamalo pomwe amapangira wuḥū kapena kusamba. Izi zimayambitsanso kunong'onezedwa ndi satana.⁵
- ❖ Mkodzo wa khanda ndi wodetsedwa ngati wa munthu wamkulu.⁶

¹ Ash-Shamāil-ul-Muhammadiyyah lit-Tirmizī, pp. 40, Ḥadīṣ 33

² Rad-dul-Muḥtār, Kitāb-uṭ-Ṭahārah, vol. 1, pp. 615


³ Al-Marja'-us-Sābiq

⁴ Fatāwā Ḥindiyyah, Kitāb-uṭ-Ṭahārah, vol. 1, pp. 50

⁵ Ad-Dur-rul-Mukhtār, Rad-dul-Muḥtār, vol. 1, pp. 613; Sunan Abū Dāwūd, vol. 1, pp. 44, Ḥadīṣ 27

⁶ Fatāwā Ḥindiyyah, vol. 1, pp. 46

- ❖ Ndi makrūh kuchita istinjā [i.e. kupeza ukhondo] ndi dzanja lamanja.¹
- ❖ Pepala silingagwiritsidwe ntchito pa istinjā ngakhale palibe cholembedwapo.²



Kulemekeza mzikiti

Okonedwa ana, mzikiti ndi nyumba ya Allah عَزَّوَجَلَّ. Ndikofunikira kuti tonsefe tiziyilemekeza.

- ❖ Zovala zanu, pakamwa panu ndi thupi lanu zonse zikhale zaukhondo ndi zonunkhira pomwe mukalowa mu mzikiti
- ❖ Ndi Haram kulowa mumzikiti ndi thupi lonunkha, pakamwa, pa zovala kapena pa chinthu china chilichonse chonunkha, chifukwa chakuti zinthu zoterezi zimakhumudwitsa angelo.
- ❖ Pangani cholinga (Niyah) cha I'tikāf nthawi iliyonse mukalowa mzikiti uliwonse. Mudzalandira mphotho kwa

¹ Al-Marja'-us-Sābiq, vol. 1, pp. 50

² Bahār-e-Sharī'at, vol. 1, pp. 611

nthawi yonse yomwe mukhala momwemo, ngakhale simuwerenga kalikonse.

- ❖ Kugona, kudya, kumwa ndi kukhala ndi kudya dakhwi komanso kufuturu sikuloledwa mu nzikiti ngati sunapange chisimikizo (Niyah) cha I'tikāf.
- ❖ Kuseka kwa chikakaka mu nzikiti kumabweretsa mdima kumanda.¹ Komabe, kumwetulira sikulakwa ngati kuli koyenera.
- ❖ Kukambitsirana nkhani zovomerezeka² mu nzikiti ndi ndi zonyasa (makrūh) ndipo kumaononga ntchito zabwino.³
- ❖ Musataye zinyalala za mtundu uliwonse mkati mwa nzikiti. Ngakhale kachinthu kakang'ono kwambiri (monga kachidutswa) kamene kali mu nzikiti kumayambitsa nzikiti kumva kupweteka monga momwe munthu amamvera akakhala ndi kachinthu kakang'ono m'diso.
- ❖ Ngati mukufuna kutenga nsapato zanu mu mzikiti, zivuleni ndi kuzimenyesa kunja musanalowe. Ngati m'miyendo mwanu muli fumbi, pukutani ndi chinthu chonga kansalu musanalowe Mzikiti.⁴

¹ Malfūzāt A'lā Ḥaḍrat, pp. 323

² An act for which, one neither gets šawāb nor punishment.

³ Faṭḥ-ul-Qadīr, vol. 1, pp. 369

⁴ Jaẓb-ul-Qulūb, pp. 257

- ❖ Kuthamanga kapena kupondaponda mapazi mu mzikiti ndikoletsedwa.¹

Ana okonedwa, lemekezani mzikiti, pewani kukambirana kosayenera, nthabwala ndi miseche, ndipo tetezani zabwino zanu kuti zisaonongeke, chifukwa ngakhale kuyankhulana kololedwa kwa za dziko mu mzikiti kumawononga ntchito zabwino za munthu.

Ulemu kwa murshid

Ngale khumi ndi ziwiri za Madanī pa ulemu wa murshid

1. Ufulu wa murshid ndi wochuluka kuposa wa bambo a munthu.
2. Bambo ali ndi ubale wathupi, pomwe murshid ali ndi ubale wa uzimu.
3. Ndizosaloledwa kwa wophunzira kuchita chilichonse chotsutsana ndi chifuniro cha murshid wake.
4. Munthu sayenera kuseka pamaso pa murshid.
5. Munthu asalankhule popanda chilolezo chochokera kwa murshid [akakhala pamaso pake].
6. Wophunzira sayenera kulabadira china chilichonse akakhala pamaso pa murshid wake.

¹ Malfūzāt A'lā Ḥaḍrat, vol. 2, pp. 318

7. Wophunzira saloledwa kukhala pomwe murshid wake amakhala, ngakhale murshid palibe.
8. Ndikofunikira kuchitira ulemu ana a murshid.
9. Ndikofunika kulemekeza zogona za murshid.
10. Ndikofunika kulemekeza tsanja zolowera m'nyumba ya murshid.
11. Wophunzira ayenera kulingalira moyo wake ndi chuma chake kukhala cha murshid wake.
12. Wophunzira sangabise kalikonse kwa murshid wake.

Kulemekeza makolo

Funso 1: Kodi makolo athu tiyenera kuwachitira chani? Kodi Allah عَزَّوَجَلَّ watilamula chani?

Yankho: Allah عَزَّوَجَلَّ watilamula kuwachitira zabwino makolo athu. Allah عَزَّوَجَلَّ wanena mu Sūrah 'Ankabūt:

وَوَصَّيْنَا الْإِنْسَانَ بِوَالِدَيْهِ حُسْنًا ط

Ndithu tatsimikizira za munthu kuti achitire zabwino makolo ake.

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira kwa Korani)] (Gawo 20, Sūrah 'Ankabūt, vesi 8)

Funso 2: Mogwirizana ndi Aḥādīš, tchulani ubwino wochitira makolo ulemu.

Yankho: Mneneri woyela صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanena kuti: 'Ngati mwana woopa Mulungu ayang'ana makolo ake mwachikondi, Allah عَزَّوَجَلَّ

amamulembera malipiro a Haji yoyankhidwa pamaso pa Allah kwa iye'.¹

Funso 3: Ndi du'ā iti imene tiyenera kuwachitira makolo athu nthawi zonse?

Yankho: Tiyenera kuchita du'ā yotsatirayi pafupipafupi kwa makolo athu:

رَبِّ اَرْحَمُهُمَا كَمَا رَبَّيْنِي صَغِيرًا

"Mbuye wanga, achitireni chisoni onse awiri monga momwe anandilera mubwana wanga."

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira kwa Korani)] (Gawo 15, Sūrah Banī Isrāīl, vesi 24)

Funso 4: Kodi tizilankhula bwanji ndi makolo athu?

Yankho: Tiyenera kulankhulana ndi makolo athu motsitsa mawu komanso mogwetsa nkhope. Tisalankhule mokweza pamaso pawo.

Funso 5: Kodi tiyenera kuwonesa khalidwe lotani kwa makolo athu?

Yankho: Tikuyenera tiwayankhe nthawi yomweyo pamene akuti itana, kuwamvera mwatcheru, ndikuwatsatira malamulo awo, ndi kupewa chilichonse chimene aletsa.

Funso 6: Kodi makolo athu amatikonda bwanji?

Yankho: Pali zabwino zambiri za makolo athu pa ife. Amatipatsa chakudya, zovala ndi maphunziro; kukwaniritsa zosowa zathu; ndi

¹ Mishkāt-ul-Maṣābīḥ, vol. 2, pp. 209, Ḥadīṣ 4944

kusamalira thanzi lathu. Choncho, tiyeneranso kuwalemekeza kwambiri.

Kulemekeza aphunzitsi

Pali mgwirizano wopatulika kwambiri pakati pa mphunzitsi ndi wophunzira. Wophunzira aziona mphunzitsi wake wachisilamu kuti ndi wamkulu kwambiri pa udindo kuposa bambo ake, chifukwa makolo amangoteteza mwana wawo ku zovuta za moyo wapadziko lapansi, pomwe mphunzitsi wachisilamu amamuteteza ku zovuta za moyo wa pambuyo pa imfa ndi Gahena.

- ❖ Ngakhale mutaphunzira chilembo chimodzi chokha kuchokera kwa mphunzitsi, mulemekezeni. Mtumiki woyela صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati: ‘Amene waphunzitsa munthu vesi imodzi ya mu Qur’an yopatulika ameneyo ndi bwana wako.¹
- ❖ Lemekeza mphunzitsi wako angakhale palibe, ndipo usakhale pampando wake.
- ❖ Ndi chiyambi chosapeza madalitso pakunamiza mphunzitsi wanu. Choncho, muzilankhula zoon nthawi zonse.
- ❖ Musayende patsogolo pa mphunzitsi wanu pamene mukuyenda naye.
- ❖ Osayang'anizana ndi phunzitsi wanu. M'malo mwake, gwetsani maso anu pamaso pake.

¹ Al-Mu'jam-ul-Kabir, pp. 112, Ḥadīṣ 7528

- ❖ Apangireni Dua makolo komanso aphunzitsi anu pambuyo pa swala iliyonse.
- ❖ Ndikofunikira kuti mulemekeze phunzitsi ngakhale samakuphunzitsani pa sukulu yanu.
- ❖ Pewani kukhala osayamika kwa aphunzitsi anu chifukwa ndi zingayambitse vuto komanso zowononga. Ngakhale zimachotsa madalitso a maphunziro. Wokonedwa Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wati: ‘Munthu amene sayamike anthu, Samayamika Allah عَزَّوَجَلَّ.¹
- ❖ Pemphani chilolezo kwa aphunzitsi nthawi zonse mukatuluka kapena kulowa m'kalasi.
- ❖ Tsatirani ndondomeko ya madrasaḥ komanso kukhala okonzeka kuchokera kunyumba yokonzedwera ndi aphunzitsi. Lankhulani phunziro lanu kwa aphunzitsi pa nthawi yake. Izi zidzamupangitsa kuti akupemphereni du’ā kuchokera pansu pa mtima pake.
- ❖ Kuvuta kwa mphunzitsi kuyenera kuwonedwa ngati n’dalitso. Pali mwambi wina wotchuka wakuti: ‘Munthu amene sanga kwanitse kupirira pakuvuta kwa mphunzitsi wake ayenera kukumana ndi mavuto m’ moyo wake.

¹ Sunan-ut-Tirmizī, vol. 3, pp. 384, Ḥadīṣ 1962

Ntchito zabwino ndi zoipa

Kunena zabodza

Kunena zomwe sizinachitike kumatchedwa bodza. **مَعَاذَ اللَّهِ عَزَّوَجَلَّ!** Kunama kwafala kwambiri m’dera lathu moti sikukuonekanso ngati choipa. Zikatero, zimakhala zovuta kwambiri kuti ana apewe kunama. Kotero tiyenera kukhomereza chidani cha kunama mwa ana athu kuyambira ali aang’ono kotero kuti akhale ndi chizolowezi cholankhula chowonadi muzikhaliidwe zonse.

Chilango cha kunama

Wokondedwa Mtumiki **صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** wanena kuti: ‘Munthu akanena bodza, mngelo amapita mtunda wa kilomita imodzi chifukwa cha fungo lake.’¹ Okondedwa, tawonani momwe kunama kuli konyansa! Pali zoipa zina zambiri za kunama.

Munthu wina anadza kwa Mtumiki ‘**إِسَاءَ عَلَيَّ نَبِيِّنَا وَعَلَيْهِ السَّلَامُ وَالصَّلَاةُ**’ nati: ‘Ndikufuna kukhala ndi inu kuti ndipeze chidziwitso cha shari’ah.’ **عَلَيْهِ السَّلَامُ** Iye anamulola, ali pawulendo anafika pa ngalande pomwe **عَلَيْهِ السَّلَامُ** anati: ‘Tidye.’ Mtumiki ‘**إِسَاءَ عَلَيْهِ السَّلَامُ**’ anali ndi mikate itatu. Onse awiri atatha kudya mkate umodzi, Mtumiki ‘**إِسَاءَ عَلَيَّ نَبِيِّنَا وَعَلَيْهِ السَّلَامُ وَالصَّلَاةُ**’ anapita kukamwa madzi mutsinje. Pa nthawi, munthuyo anabisa mkate wachitatu. Atabwerera, Mtumiki ‘**إِسَاءَ عَلَيْهِ السَّلَامُ**’ anafunsa: ‘Kodi mkate wachitatu uli kuti?’ Munthuyo ananena boza kuti, ‘Sindikudziwa.’ Mneneri ‘**إِسَاءَ عَلَيْهِ السَّلَامُ**’ sananene kalikonse. Patapita nthawi, iye **عَلَيَّ نَبِيِّنَا وَعَلَيْهِ السَّلَامُ وَالصَّلَاةُ** anati: ‘Tiyeni.’

¹ Sunan-ut-Tirmizī, Kitāb-ul-Bir-Waṣ-Ṣalāh, vol. 3, pp. 392

Ali m'njira, anaona nswala ndi ana ake aamuna awiri. عَلَيْهِ السَّلَامُ anaitana nswalayo imodzi yomwe inadza kwa iye, ndipo kenako anaipha ndi kuiotcha, ndipo onse awiri anadya pamodzi. Atamaliza kudya, Mtumiki Īsā عَلَيْهِ السَّلَامُ anasonkhanitsa mafupa a nkhosayo nati, 'قُمْ بِأَذْنِ اللَّهِ' (Ndithu, dzuka kwa akufa ndi lamulo la Allah عَزَّوَجَلَّ). kwa amayi ake. Pambuyo pake, Mtumiki isa عَلَيْهِ السَّلَامُ anati kwa munthuyo: 'Ndikulumbiritsa iwe m'dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ Amene wandipatsa mphanvu yosonyeza chozizwitsa ichi. Nenani zoonā; Mkate wachitatu uja uli kuti?' Munthu uja anayankhanso kuti: 'Sindikudziwa.' Mneneri Īsā عَلَيْهِ السَّلَامُ anati: 'Tiyeni tipite patsogolo

Pamene anayenda patsogolo, anafika pamtsinje pomwe عَلَيْهِ السَّلَامُ anagwira dzanja la munthuyo napitiriza kuyenda pamodzi amtsinjewo kufikira anawoloka ndi kukafika tsidya lina. Pambuyo pake, عَلَيْهِ السَّلَامُ anati kwa munthuyo: 'Ndikulumbiritsa iwe m'dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ Amene wandipatsa mphanvu zosonyeza chozizwitsa ichi. Nenani zoonā; Mkate wachitatu uja uli kuti?' Munthu uja anayankhanso kuti: 'Sindikudziwa.' Mneneri Īsā عَلَيْهِ السَّلَامُ anati: 'Tiyeni.

Pamene anayenda patsogolo, anakafika kuchipululu komwe Mtumiki Īsā عَلَيْهِ السَّلَامُ anaunjikira mchenga ndi kunena kuti: "E iwe mulu wa mchenga! mbali zitatu ndi kunena kuti: 'Chigawo chimodzi ndi changa, china ndi chako, chachitatu ndi cha amene watenga mkate wachitatu.' Munthuyo atanva zimenezi nthawi yomweyo anati: 'Ndine amene ndinatenga mkatewo. mtanda wachitatu wa mkate.'" Atanva izi, Mneneri Īsā عَلَيْهِ السَّلَامُ anati, Tengani golide yenseyu.

Atanena izi, عَلَيْهِ السَّلَامُ anamusiya munthuyo. Munthuyo anasangalala kwambiri atalandira golide wambiri. Atakulunga golideyo m'nsalu,

munthuyo anapita patsogolo. Ali m’njira anakumana ndi anthu ena awiri. Awiriwa anaona kuti munthuyo anali ndi golide ndipo ankafuna kumupha, koma anatha kuwaletsa powauza kuti golideyo agawidwe m’zigawo zitanu ndi kugaŵidwa kwa iwo mofanana. Zimenezi zinkaoneka kuti zinawakhutiritsa anthu awiriwo. Kenako anati: ‘Mmodzi wa ife apite kumzinda wapafupi ndi golide wochepe n’kukagula chakudya kuti tisangalale ndi chakudya chokoma tigawana golide pambuyo pake.’ Choncho, mmodzi wa iwo anapita mumzinda wina kukagula chakudya. koma chifukwa cha umbombo wake, anaikapo poizoni m’chakudyacho kuti amuna awiri aja afe, ndipo iye anatenga golide yenseyo. Chomcho anagula poyizoni n’kusakaniza m’chakudyacho.

Kumbali ina, awiri enawo anali atakonza kale chiwembu choti amuphe akangobwerako kuti agawane golideyo mofanana. Atabwera ndi chakudya, onse awiri anamupha mwankhanza. Zitatha izi, anadya mosangalala chakudyacho, chomwe chinali ndi poizoni. Chotsatira chake chinali chakuti amuna awiri aja nawonso anafa akupiringizika, ndipo golideyo anakhalabe mmenemo.

Pamene Mneneri *عَلَىٰ نَبِيِّنَا وَعَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ* ‘Īsā anabwerera pamodzi ndi maswahaba ake nakumana ndi mitembo yakufayo, analoza golide ndi matupi a anthu atatuwo nati: “Taonani zowona zake za dziko lapansi! Nkoyenera kwa iwe kuti ukhale kutali ndi ilo.”¹

Ana okondedwa, mwaona kuti kunama ndi kukonda chuma cha dziko zinamuononga bwanji munthuyo? Sanapeze chumacho, ndiponso

¹ Ithāf-us-Sādat-il-Muttaqīn, vol. 9, pp. 835

Sanapindule chilichonse. Kuwonjezera pa kutaya moyo wake, iyenso anataya moyo wake pambuyo pa imfa.

*Na mujh ko āzmā duniyā kā māl-o-zar ‘aṭā kar kay
‘Aṭā kar apnā gham aur chashm-e-giryān yā Rasūlallāh*

*Chonde musandiyese pondipatsa chuma Chadziko lapansi
Ndidalitseni ndi kudzipereka kwa Inu ndi maso akulira, E, Mtumiki wa Allah*

Zoipa zina za kunama

Sayyidunā Bakr Bin ‘Abdullāh رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ wanena kuti panali munthu wina yemwe anali kupita mabwalo amafumu ndikuwapasa malangizo. Posangalalaye, mafumuwo akam’patsa mphoto ndi kumulimbikitsa.

Nthawi ina anapita ku bwalo la mfumu n’kunena kuti akufuna kupereka malangizo. Mfumuyo inamulola kuti akhale pampando umene unali kutsogolo kwake n’kumupempha kuti alankhule. Mlangiziyo anati: ‘Bwezerani chisomo ngati wina wakukomerani mtima, ndipo amene wakuchitirani choipa azakumana ndizotsatira zake popanda inu kumuchitira choipa chilichonse.’ Mfumuyo itasangalala ndi kunva zimenezi, inamwadza mphoto. Mkulu wina wa kuchifumu ataona zimenezi anachita nsanje chifukwa cha nyota imene mfumuyo inapereka kwa munthu wamba. Atagwidwa ndi nsanje, iye anapita kwa mfumuyo n’kumunamiza m’njira yosyasyalika kuti: ‘Wolemekezeka !Ngakhale kuti munthu ameneyu wakupatsani malangizo abwino, amadana nanu ndipo akunena kuti mfumu ili ndi mpweya woipa.’ Mfumuyo itanva zimenezi inafunsa kuti: ‘Kodi uli ndi umboni wosonyeza kuti wanena zimenezi?’ Munthu wansanjeyo anayankha kuti: Ukulu! Ngati mukukaikira, chonde muyitaneni ndikumupempha kuti ayandikire kwa inu. Akayandikira, adzaika

dzanja lake pamphuno chifukwa cha fungo la m'kamwa mwanu.' Mfumuyo itanva zimenezi inati: 'Sindingasankhe zochita pokhapokha nditafunsa ndekha za nkhaniyi. Atachoka m'bwalo lachifumu, munthu wansanjeyo anapita kunyumba ya phungu uja ndi kumuitanira kunyumba kwake kuti akadye chakudya. Iye anavomera ndipo anapita kunyumba ya munthu wansanjeyo. Chakudya choperekedwa ndi munthu wansanjecho chinali ndi adyo wochulukwa.

Chifukwa cha kudyachi, mlangizi anali ndi mpweya woipa. Komabe, anabwerera kunyumba. Patangopita nthawi pang'ono, mthenga wochokera kwa mfumu anabwera kudzausa mlangizi kuti mfumu ikumuyitana nthawi yomweyo. Chotero, iye anafika ku bwalo lachifumu limodzi ndi mthengayo. Pomulola kuti akhale pampando kutsogolo kwake, mfumuyo inamupempha kuti abwerezenso malangizo omwe anamupatsa dzulo. Iye anati: 'Bwezerani chisomo ngati wina wakuchitira zabwino, ndipo amene wakuchitirani choipa adzakumana ndi zotsatira zake popanda iwe kum'chitira choipa chilichonse.' Pambuyo pake, mfumuyo inampempha kuti ayandikire pafupi. Atafika pafupi ndi mfumuyo, anaika dzanja lake pakamwa kuti mfumu isanyansidwe ndi fungo la m'kamwa mwake. Mfumuyo itaona zimenezi, inaganiza kuti mnyamata wake anamuza zowona. Mfumuyo inakhala ndi maganizo olakwika pa iye ndipo inaganiza zomulanga kwambiri mopanda kusamala zakufufuza kulikonse. Mfumuyo inalemba kalata kwa bwana mkubwa ndi lamulo ili: 'Munthu uyu akafika kwa inu ndi kalata yanga, mumuphe ndipo munditumizire khungu lake lodzaza ndi mankhusu.' Atasindikiza kalatayo, anaipereka kwa mfumu. phungu, ndipo mfumu inamupempha iye kuti apite kwa kazembe wa wakuti-ndi-wakuti.

Chinali chizolowezi cha mfumu kutumiza munthu ndi kalata yosindikizidwa yake kwa bwana mkubwa wa mzinda uliwonse kuti wonyamula kalatayo apatsidwe mphotho. Mfumuyo inali isanalebepo kalata yolanga aliyense. Aka kanali koyamba kuti achite zimenezi.

Pamene mlangiziyo anatuluka m'bwalo lachifumu, munthu wansanjeyo anali kumudikirira uku akupumira mwamba. Atafika kwa iye, munthu wansanjeyo anamufunsa chimene chinachitika ndi kumene ankapita. Iye anayankha kuti, 'Pamene ndinapereka uphungu womwewo kwa mfumu, inandipatsa kalata yosindikizidwa ndi kundipempha kuti ndipite kwa kazembe wakuti-ndi-wakuti. Tsopano ndikupita kukakumana ndi bwana mkubwa.' Munthu wansanjeyo anati: 'M'bale! Ndikapereke kalatayi kwa bwana mkubwa.' Mlangiziyo anapereka kalatayo kwa iye. Munthu wansanjeyo anapita ku nyumba ya bwana mkubwa mosangalala. Iye ankaganiza kuti ananyenga mlangiziyo ndipo tsopano adzalandira mphoto ndi mphoto kuchokera kwa bwanamkubwa, koma sankadziwa kuti adzakumana ndi chilango chake.

Atafika kunyumba ya bwanamkubwa, anapereka kalatayo kwa bwanamkubwa mwaulemu. Powerenga kalatayo, bwana mkubwayo anafunsa kuti: 'Kodi mukudziwa lamulo limene mfumu yandipatsa kudzera m'kalatayi?' Iye anayankha kuti: 'Wolemekezeka! Mfumuyi iyenera kuti inakulamulani kuti mundipatse mphoto.' Bwana mkubwa anati: 'Iwe munthu wopanda nzeru! Wandilamula kuti ndikuphe ukangofika kuno ndi kutumiza khungu lako lodzaza ndi mankhusu kwa iye.' Anachita mantha kunva zimenezi, munthu

wansanjeyo anati: ‘Ndikulumbirira Allah عَزَّوَجَلَّ! Mfumu sinapereke lamuloli kwa ine, koma kwa munthu wakuti-ndi-wakuti. Mungafunse za nkhaniyi mwa kutumiza mthenga kwa mfumu.’ Ponyalanyaza pempho lakelo, bwana mkubwayo anati: ‘Sitifunikira kufunsa. Tiyenera kuchita monga mwalamulo la mfumu monga momwe kalatayo ili ndi chidindo chake.’ Chotero bwana mkubwayo analamula wopha kuti aphe munthu (wansanje), kuchotsa chikopa chake ndi kudzadza mankhusu mmenemo. Kenako, mtembo wake unatumizidwa kwa mfumu.

Tsiku lotsatira, phunguyo anapita ku bwalo la mfumu monga mwa nthawi zonse ndipo anabwereza uphungu womwewo pamene anaima pamaso pa mfumu: ‘Bwezerani chisomo ngati wina wakuchitirani zabwino, ndipo amene wakuchitirani choipa adzakumana ndi zotsatira zake popanda inu kumuchitira choipa chilichonse’. Mfumuyo itamuona ali moyo, inafunsa kuti: ‘Bwanji za kalata imene ndakupatsani?’ Iye anayankha kuti: ‘Ndinakumana ndi munthu [wansanje] uja pa ulendo wanga wopita ku nyumba ya bwana mkubwa. Anandipempha kuti ndimupatse kalatayo, ndipo ndinamupatsa; anapita nayo kwa bwana mkubwa.’ Mfumuyo inati: ‘Anandiuza kuti ukuganiza kuti ndili ndi mpweya woipa. Kodi n’zoona?’ Iye anayankha kuti: ‘Mfumu! Sindinakhalepo ndi maganizo oterowo ponena za inu.’ Mfumuyo inafunsa kuti: ‘N’chifukwa chani unayika dzanja lako pakamwa pako pamene unafika pafupi ndi ine dzulo?’ Iye anayankha kuti: ‘Mfumu, ndisanabwere kunyumba yanu yachifumu, ndinapita kunyumba kwake chifukwa anandi itanira chakudya. Anawonjezera adyo wambiri pa chakudyacho, motero, ndinali ndi fungo loipa. Popeza sindinkafuna kuti mukhale

osamasuka chifukwa cha fungo la m’kamwa mwanga, ndinaika dzanja langa pamenepo.’

Mfumuyo itamva zimenezi inati: ‘Iwe munthu wamwayi! Malangizo amene munandipatsa ndi owona. Munthu wansanje uja ananamiza kuti akulangizeni koma ananyamulidwa ndi nsanje yakeyo n’kukumana ndi chiwonongeko chake. Iwe munthu woopa Mulungu! Khala pamaso panga ndi kubwerezanso uphungu womwewo.’ Chotero, iye anakhala pamaso pa mfumu nati: ‘Bwezerani chisomo ngati wina wakukomera mtima, ndipo amene wakuchitira choipa adzakumana ndizotsatira zake popanda iye kumuchitira choipa chilichonse.’

Okondedwa ana

- ❖ Amene amachitira chifundo ena amachitiridwa ubwino ndi ena, ndipo amene amayambitsa vuto kwa ena amapatsidwa vuto ndi ena.
